April – June 2018

www.ccog.org

# Nkhani Za Ulosi M Baibulo

## Kodi Mpingo Woona Wa Mulungu Ndi Woyenera Kukhala Ndi Likulu Lake Ku Yerusalemu?

*Anthu ena akumatero.*
*Kodi  nanga baibulo likutiphunzitsa kuti chiyani?*


**Kodi chipangano chakale chikutiphunzitsa chiani za Ufumu wa Mulungu?**

**Sitidzathawa CHITSAUTSO Cha Chikulucho**




# BIBLE NEWS PROPHECY



3



6



15


16

# M'magazini Ino:

3 **Kuchokera Mkonzi: KODI MPINGO WOONA WA MULUNGU NDI WOYENERA KUKHALA NDI LIKULU LAKE KU YERUSALEMU?** Anthu ena akumatero. Kodi nanga baibulo likutiphunzitsa kuti chiyani?

13 **TIYENI TIWERENGE PHUNZIRO 13 LA BAIBULO: Kodi cholowa cha Akhristu chiani?** Kodi akhristu adzalandira cholowa chawo pa dziko lapansi kapena kumwamba?

28 **Kodi chipangano chakale chikutiphunzitsa chiani za Ufumu wa Mulungu?** Kodi ana Aisraeli amadziwa za Ufumu wa Mulungu kuchokera mu malemba a chihebri?

31 **SITIDZATHAWA CHITSAUTSO CHA CHIKULUCHO!** Mtumiki wakale Leroy Neff analemba zokhuzana ndi nkhaniyi zaka zapitazi. Matsiku alerowa zili kutsonyeza kuti tili mu nthawi ya zitsautso zazikulu.

**CHIKUTIRO CHA KUNJA: intaneti ndi wayilesi** zikusonyeza mene mungapedzere ma mauthenga kuchokera mu Mpingo woona wa Mulungu.

**Pa Tsamba Loyamba:** Dulani chithunzi chojambulidwa ndi Dr. Bob Thiel wa ku Yerusalemu.

**Nkhani za Ulosi wa baibulo (nyuzipepala) zimalembedwa ndi a Mpingo wa CONTINUING CHURCH OF GOD, 1036 W. Grand Avenue, Grover Beach, CA, 93433. http://www.ccog.org**

**©2018 Continuing Church of God. Printed in the U.S.A. All rights reserved.**

**MKONZI WAMKULU: Bob Thiel**

**WOTHANDIZIRA: Joyce Thiel, John Hickey; SBC Course Assister: Shirley Gestro.**

**WOMASULIRA MU CHICHEWA: RADSON MULOZOWA, MOSES CHIMPHANGWI, PRISCILLA MONIWA**

**Kupanga:** James Erwin EStoque

# Kuchokera Mkonzi: BOB THIEL



## KODI MPINGO WOONA WA MULUNGU NDI WOYENERA KUKHALA NDI LIKULU LAKE KU YERUSALEMU?

Ena akhala akunenena kuti  Mpingo wa Mulungu woona ndi woyenera kukhala  ndi likulu lake ku Yerusalemu.

Kodi nanga Baibulo limatiphunzitsa chiani?

Mu zaka zambuyo yemwe anali Mtsogoleri wa Church of God Seventhday, Malemu AN DUGGER, anayambitsa gulu lake lotchedwa TIBWERERE KU YERUSALEMU.

Dugger kudzera mu gulu lake anatsimikidzira anthu kuti Yerusalemu ndi mzinda okhawo umene Mpingo woona wa Mulungu ungakhazikitsidwe. Mwa ich iye anapita ku Yerusalemu nakhazikitsa ofesi yake.

Koma zoona zake ndi zoti Yerusalemu anali Malo okhawo amene kumachitikira zinthu zosiyanasiyana monga kutsindikiza ma bukhu komanso zidindo.

Mu chaka cha 2015 Dr Bob anakwanitsa kuyankhula ndi amene anali Mtsogoleri wa Church of God Seventhday (CG7), ROBERT COULTER  za nkhaniyi.  Coulter ndi Mtsogoleri amene analemba mbiri ya Church of God Seventhday.

> Iye ananditsimikizira kuti  Dugger sanali kudziwa zambiri ya Yerusalemu mwakuya ayi koma amangoyerekeza pogwiritsa ntchito Yerusalemu ngati malo ofunikira kwambiri pa zochitika zonse.

Mu zaka za ma zikwi 20 tikuwona zinthu zina zofanana ndiko kukhazikitsidwa kwa gulu lina  ku Yerusalemu lotchedwa  7th Day Church of God. Gululi  linakhazikitsa likulu lake ku Yerusalemu ndi cholinga chokhazikitsa chikhulupiriro choona pa dziko lapansi, ndipo linafalikira malo osiyanasiyana.  Madera onse anali kupereka mapempho awo ku Yerusalemu.

Mu chaka cha 1970 Mtumiki  AM SHOEMAKER, anatumizidwa kupita ku Kenya, Africa  kukayankha mafunso okhunzana ndi nkhaniyi.  Patangotha miyezi iwiri anabatiza anthu 284 Ndipo Anadzodza anthu 16 mu utumiki ndipo analandira Ubatizo wa Mzimu Woyera.

YERUSALEMU MESSANGER:  Gululi linanakhadzikitsidwa ku Yerusalemu ndipo limapereka ndondomeko, zithunzi za magulu onse amene amagwira nawo ntchito, komanso kukonda Yerusalemu pa dziko la pansi. (Masalmo 28:5, 6).

Pali magulu osiyana siyana maiko ndi madera amene akhala akutenga mbali pa ntchito yabwino yolemba mabukhu kuchokera ku likulu lawo. Monga likulu lina liri ku Denver,Colorado, Meridian,Idaho  amene amapereka Uthenga wa choonadi  ( Miyambo 30:4, Masalmo 68:4, 91:14, 69:35,36. Yesaya 52:6) amene amapezeka  ku Oregon,

Mzinda wa JUNCTION, komanso ALABAMA ,mu Mzinda wa JACKSON GAP komanso ku MICHIGAN (The faith of holt),

**Tili kukhulupirira kuti zonsezi zikugwa mundondomeko wa kuyankhula kwa malembo oyera pamene gulu la anthu likutsimikiza kuti Mzinda wa Yerusalemu unasankhidwa ndi Mulungu Atate ndipo uyenera kudzindikirika kuti likulu pa dziko lonse lapansi kwa onse osankhidwa otsalawo agwire dzina la chipangano mwa chikhulupiriro choona chimene chinapatsidwa kamodzi kwa oyera mtima omwe akutsogozedwa ndi mzimu woyera.** (http // jsdccog. org/a brief history/02/8/17 ).

Kodi Atate anasankha Yerusalemu kukhala ofesi yaikulu ya Mpingo wa Mulungu mu mbadwo uno kupyolera malembo oyera monga tamvera poyamba paja?

Ayi.

Choyambirira ndiloleni ndifotokoze kuchokera mu bukhu la Chibvumbulutso 12: 17 lomwe likufotokoza za kutsagwirizana kwa Akhristu matsiku otsiriza, ndipo vesiyi silikunena kanthu za Mzinda wa Yerusalemu lingakhale



amodzi mwa iwo.

Ndinatsimikidzira izi ndi mkulu wina wa Mpingo wa Mulungu ( Seventhday, Denver ) a LOREN STACEY PA 21 Desembala 2017, siokhawo kumeneko palinso gulu lina lotsogoleredwa ndi a ROGER BONNE ndinawatsimikizira chimodzi modzi mgulu lawo lotchedwa ( MERIDIAN REFERENCED CHURCH ) tsiku lomwelo la pa 21 Desambala 2017.

Gulu la ku Yerusalemu likungowonetsa kudziwa kwao za likululo koma sakuziganizira mwa okha kuti adziwe kuti malowo iwonso sakuwakhuza bwanji, pakuganizira kuti malowo ndi oyera.

Gulu lozungulira Yerusalemu likungoona malowo kukhala likulu la kumeneko koma sakudziwa kuti iwowo malowo awakhuza bwanji. Kuwonjezera apa magulunso ena pakuyesa malowo kuti ndi oyera kutsiyana ndi magulu ndatchula pa mwambapa. Kunena za Denever,Meridian makamaka anthu ndawatchulawa mu mumpingo imeneyo sanamvepo za Yerusalemu Seventhday Church of God.

**CHACHIWIRI:** Baibulo limaonetsa kuti Mzinda wa Yerusalemu sunasankhidwe ndi Atate kuti ukatsogolere ntchito yake yokhulupirika.

**CHACHITATU:** Nyumba yoyamba ya Yerusalemu sili mmanja mwa Mpingo wa Mulungu,iri mmanja mwa Ayuda, ndipo Mpingo wa ku Roma ukufuna nyumbayi. Ndipo mu nthawi yina Asilamu akhala akugwiritsa nyumbayi.

Chikuonekachi ndi Chinthunzi cha nyumba zina chimene ndinajambula nditapita ku Yerusalemu zaka zingapo zapitazi. Palibe mpingo woona wa Mulungu ukuyembekezera

kugwiritsa ntchito nyumbayi.

Chinthunzi cha njerwa zoyambirira ndi zimene zinagwiritsidwa ntchito pomanga nyumbayi. (chinthunzichi chikuonekanso pa chikutiro cha nyimbo zimene ife a CCOG timagwiritsa ntchito). Ife tili kupitiriza Chikhristu choyambacho chimene chinayambika ku Yerusalemu ndipo kenako chinasamukira ku Antiokeya, Asia minor, kenako likululo linasamukira ku Europe kwawo kwa Azungu kenako ku mayiko aku Madzulo a dziko la USA.

Izi sidzikuthathauza kuti kulibe malo ku Yerusalemu, koma baibulo silinena kuti Yerusalemu kukhala likulu loyamba la anthu omwe amasunga chikondi cha pa abale(Philadelphia) ngati chitsanzo cha Mpingo wa Mulungu woyamba.

**CHACHINAI:** Ambuye Yesu akuonetsa poyera kuti Akhristu ayende mizinda yambiri kulalikira uthenga wabwino kuyambira ku Israeli, iye asanabwere. Mateyu 10:23 sikufotokoza kuti likulu la utumikiwu kukhala ku Yerusalemu.

**CHACHISANU:** Mtumwi Yohane anali modzi mwa oyambawo ndi otsiriza kumwalira koma munthawi yake amatumikira ku Aefeso osati ku Yerusalemu. Yohane sanaphunzitse kuti ku Yerusalemu kungakhale likulu. Pamene ambuye Yesu amamutuma yohane kulemba bukhu lotsiriza la mu baibulo panali makalata opita ku Mipingo isanu ndi iwiri yak u Asia, panalibe kalata inatumidzidwa ku Yerusalemu. Kuwonjezera apo atamwalira Yohane, Polycarp anatsogolera okhulupirira a ku smyra osat a ku Yerusalemu.

**CHACHISANU NDI CHIMODZI:** Pangono pangono pamene Yerusalemu imatchepa mphamvu yakukhala ndi atsogoleri a chiyuda mu zaka 135 AD.

Ambuye atabadwa mu mzindawu palibe akanapitiriza Mpingo wa Mulungu owonawo kwa kanthawi choncho kunakhazikika ulamuliro wa Ufumu wa CHIROMA. (Gibbon and Decline and fall of….)

Akhristu a mpingo woona wa Mulungu sanali kuloledwa kutumikira ku Yerusalemu chitadutsa chaka cha 135 AD. Malingana ndi anthu otchedwa Airenius mu chaka chachiwiri Ambuye atabadwa 2 AD, ku Yerusalemu kunatsiya kutulutsa zipatso zeni zeni za Mpingo woona wa Mulungu. (Adversus heareses book iv (4) chapter iv verse 1.

**CHACHISANU NDI CHIWIRI:** Ngakhale Akhristu owoona anabwerera nthawi ya kulamulira kwa Mfumu Consitantine ndi Theodosius, Mpingo wa Mulungu unaletsedwa ndi Mafumu a chiroma ku Yerusalemu ,nalamulira kuti yense wakuphunzitsa chiphunzitso chimenecho aphedwe, makamaka wakuletsa kudya mkhumba. Nayo Mfumu Theodesius analamulira imfa pa Akhristu omwe amasunga Pasaka matsiku oyenera kalendala ya Chiyuda (pa 14 mwezi wa Nissan, mkati kati mwa mwezi wa epulo komanso Marichi).

Yerusalemu sunali likulu la Mpingo woona wa Mulungu monga mene mbiri ikunenera ndi kusonyeza. Munthawi imene ndinakacheza ku Yerusalemu Ndiloleni ndinene kuti kuyankhula kwa ufulu pa chipembezo,luso la makono lolumikizirana pa dziko lonse. America ndi dziko lokhalo likukwaniritsa malemba pa kulalikira monga mwa mawu apa Mateyu 24:13 komanso Mateyu 28:19-20.

## MALEMBO OYERA

Kodi nanga Malembo Oyera akuti chiyani?

Baibulo likuphunzitsa vesi

10. Tiri nawo guwa la nsembe limene iwo akutumikira Chihema alibe ulamuliro wakudyako. Pakuti matupi a nyama zija, mwazi wa izo unatengedwa ndi mkulu wa nsembe kulowamalo opatulidwa, chifukwa cha zoipa ,amatenthedwa kunja kwa msasa. mwaichi Yesunso. kuti akayeretse anthuwo mwa mwazi wa iye yekha adamva chowawa kunja kwa chipata. Chifukwa chake titulukire kwa iye kunja kwa tsasa osenza tonzo lake. Pakuti pano tilibe mudzi wokhalitsa komatu tifuna funa ulinkudzawo. (Ahebri 13:10 -14 )

Choncho mawu awa akutitsimikizira kuti palibe mzinda umene wakhazikika ngati likulu la Akhristu omasulidwa. Monga Jamieson, Brown ndi Fausset anapitiriza kufotokoza za Yerusalemu.

Yesu anaphunzitsa kuti pamene angakunzunzeni inu mudzi uwu, Thawirani wina, indetu indetu ndinena ndi inu, simuzatha mizinda ya Israeli kufikira mwa wa munthu atadza. ( Mateyu 10:23).

Masautso atafika kwa akhristu ku Yerusalemu iwowo anathawa ndipo mawu a Mulungu sakunena kuti Akhristu anathawawo anabwerera kumene anathawako. Mawu a Ambuye Yesu pa Mateyu 10:23 akutsimikidzira zimene zinachitika pa mbiri ya mpingo woyamba . Akhristu anathawa ku Yerusalemu napita ku Pella mu zaka za 67 AD pamene ena anabwereranso mu zaka za 135AD. Zoona zake zoti mbiri ikunena kuti mtumwi Filipo ndi Yohane anapita ku Asia Minor.

Tatiyeni tione 1 Akorinto 12:28. Ndipotu Mulungu anaika ena mu Mpingo,poyamba atumwi, achiwiri aneneri, achitatu Aphunzitsi, pamenepo zozizwa,pomwepo mphatso za matchiritso, mathandizo, maweruziro, malilime a mitundu mitundu.

Popeza kuti atumwi anali oyamba Mulungu kuwapatsa mphamvu ya kutsogolera Mpingo, ngakhale mtumwi Yohane anachoka pakati pa atumwi kukakhala ku Asia Minor yekha. Uku kunali kuonetsa kuti sanakhulupirire kutsata chiphunzitso chonyenga motero sanafune kukhazikika ku Yerusalemu ngakhale omutsatira wake anachita chimodzi modzi.

Ena amene akunena kuti Yerusalemu ndi mzinda wa Mpingo wa Mulungu mu mbadwo uno akuloza mawu opezeka pa Yesaya 2:2,3,4, ngati chidziwitso choona.

Tiyeni tiyangane za lembali pa mutu 2 :2_4. Ndipo padzakhala masiku otsiriza kuti phiri la nyumba ya Yehova lidzakhazikika pa msonga la Phiri, ndipo lidzakwedzedwa pamwamba pa zitunda: mitundu yonse idzasonkhana komweko. Ndipo anthu ambiri adzanka nati; tiyeni tikwere kunka kuphiri la Yehova kunyumba ya Mulungu wa Yakobo, ndipo adzatiphunzitsa za njira zake, ndipo tidzayenda mu mayendedwe ake, chifukwa mu Ziyoni mudzatuluka chilamulo chake, ndi mau a Yehova kuchokera ku Yerusalemu. Iyeadzaweruza za pakati pa akunja, adzadzudzula mitundu yambiri ya anthu, ndipo iwo adzasula malupanga awo akhale zolimira, ndi nthungo zawo zikhale makasu, mtundu sudzanyamula lupanga kumenyana ndi mtundu wina ndipo sadzaphunziranso nkhondo.

Tatiyeni tione mfundo zina kuchokera mu bukhu la Zakariya.

> Zekariya 1: 16,17. Chifukwa chake atero Yehova, ndabwera kudza ku

Yerusalemu ndi zachifundo,nyumba yanga idzamangidwamo, atero Yehova wamakamu, ndipo adzayetsa Yerusalemu ndi chingwe. Fuulanso ndi kuti atero Yehova wa makamu: midzi yanga idzalemera ndi kufalikiranso: ndipo Yehova adzatsangalatsanso Ziyoni, nadzasankhanso Yerusalemu.

Zekariya 2: 10-13. Imba nukondwere, mwana wa mkazi wa Ziyoni,pakuti taonani ndilinkudza ndipo ndidzakhala pakati pawo ati Yehova. Ndipo amitundu ambiri adzaphatikidzidwa kwa Yehova tsiku ilo,nadzakhala anthu anga, ndipo ndidzakhalapakatipako,ndipoudzadziwa kuti Yehova wa makamu ananditurna kwa iwe. Ndipo Yehova adzalandira cholowa chake Yuda, ngati gaawo lake mu dziko lopatulika,nadzasakhanso Yerusalemu. Khala chete, anthu onse, pamaso pa Yehiva, pakuti wagalamuka mokhalira mwake mopatulika.

Munthawi imeneyo Aneneri amaonetsa kuti nthawi izafika imene Mulungu adzasankhanso Yerusalemu, komanso kuti sidzichitika posachedwapa koma nthawi ya mtsogolo. Monga zanenedwa kale lingalirani kuti Baibulo likuphunzitsa kuti pali mipingo isanu ndi iwiri kuchokera ku Aefeso kupita ku Laodikaya. Mipingo yonseyi isanu ndi iwiri inakhazikika ku Asia Minor ndi ina imene ilipo sikuonetsa kapena kufoyokoza za Yerusalemu. Koma Ambuye akanafuna kuti likulu mpingo wake likhale ku Yerusalemu akanayenera kutsimikidzira.

Yesaya 2: Sikufotokozanso kuti Akhristu ambiri adzakhala ku Yerusalemu pa nthawi yothawa chisautso chachikulu chimene chili kubwera.

Chibvumbulutso 12:14-17, Mateyu 24:16-17. Baibulo silifotokoza kuti Mpingo udzakhazikika ku Yerusalemu mu nyengo ino. Yesu anatiphunzitsa kuti mudzawadziwa iwo ndi zipatso zawo (Mateyu 7:) monga zipatso za ku Yerusalemu.

## ZIPATSO NDI NTCHITO ZA KHRISTU NDI ZIMENE ZIKUFUNIKA OSATI MALO OPEMPHERERA.

Palibe gulu la Mpingo limene likutsimikizira kuti Mpingo wa Mulungu woona uyenera kukhala ndi likulu lake ku Yerusalemu pofuna kukwaniritsa mawu a pa Yesaya 2. Iwo amatsindikiza kuti mawu Ambuye ayenera kuchokera ku Yerusalemu.


Miyambo 28:14 Wodala wakuopa Yehova kosalekeza, koma woumitsa mtima wake adzagwa mu zoipa.

Ife a mpingo wa CCOG tichite nawo molakwitsa. tawonapo anthu akutumikira kumanena kuti iwo ndi ma Filadefiya amene amasonyeza ngati akutsatira ndi kuphunzitsa choonadi cheni cheni pamene ndi Afarisi oyamba aja amene amanena kuti atero ambuye pamene zimachokera mu maganizo awo.

Ife a CCOG tikuphunzitsa ndi kutsogolera zimene tikuona kuti ndi nchito yoyenera matsiku otsiriza moga ma Filadefiya amene akutchulidwa pa Chibvumbulutso 12: 14 – 17.

Ndikulakwitsa kunena kuti Mpingo woona wayenera kupezeka ku Yerusalemu. Amene akufuna kukhala ngati Akhristu a ku Filadefiya (Chibvumbulutso 3: 7-13) ayenera kudziwa za malembo oyera posatengera za Nkhani ya Yerusalemu.

# MAPHUNZIRO A MU BAIBULO




## MUTU 13: KODI AKHRISTU ADZALANDIRA CHIYANI?

Tinabadwa Dziko limene liri ndi zochitika zambiri koma pamene tinabadwa sitinadziwe kanthu ,choncho titakula tinayamba kuona zochitika zimene tinayamba kudzigwiritsa mmaganizo athu kufikira zinakhala khalidwe lathu.Mwakutero tinayamba kutsatira zikhalidwe za dziko mosayanganira choona cake cheni cheni. Ena anali abwino koma ambiri a iwo anali oipa. Baibulo likutiphunzitsa kuti.

> Taonani ichi chokoma ndachipeza kuti Mulungu analenga anthu oongoka mtima, koma iwowo afunafuna malongosoledwe amitundu mitundu. (Mlaliki 7:29).

Anthu analengedwa oongoka koma munthu ayesedwa pamene chilakolako cha iye mwini chimkokera ndikumunyenga. ( Yakobo 1:14 )

Palibe mmodzi wolungama. ( Aroma 3: 10).

Ndinabadwa ndi chikhalidwe ndipo timanena kuti ndi chilengedwe. Ndi anthu ochepa amene amadziwa za izi. Pa chilengedwe cha munthu pali mbali ya uzimu ndi kuthupi.

Kumbali ya thupi pali zinthu zimene tiyenera kudzidziwa monga kutentha thupi, kumva ludzu, zokhumba za thupi, kusewera masewero. Zina mwa izi zimatikokera ku ntchito zopanda pake monga madano,umbombo ndeu. Mwaichi chilengedwe cha Munthu chinasanduka chikhalidwe ndi cholinga choti satana alande mphamvu ndi chikhalidwe cha anthu. (Ana sakumvera malamulo a makolo).

Tinakula ndi makhalidwe ozichepetsa pansi pa ulamuliro chomwecho tiyenera kutero ndi mulungu. Chikhalidwe cha munthu chayenera kukhala chabwino nthawi zonse osati pokha pokha ukakumana ndi mavuto.

Malamulo a mulungu amatitsogolera ku zinthu zosaoneka monga chikondi pa mulungu, kumudalira ndi kumvera malamulo komanso chitsogozo cha mulungu nthawi zonse.

Pokhala nawo mtima womvera, kudalira mulungu, kumulambira, chikhulupiriro, chikondi pa wina ndi zake, izi zimawonetsa kuti ndife ofanana ndi iye mwini. Popeza izi sidzichokera mumaganizo a munthu koma kwa atate amene amapereka kwa omumvera iye.

Chikondichi chikabwera pa munthu ngati mphatso ya mzimu woyera chimamuthandidzira munthu kukhala wa mtendere, chimwemwe, chikondi pa abale, kutsangalara nthawi zonse. Palibe angachitike izi popanda mzimu woyera ngakhale chikondi ndilo lamulo lochokera kwa Mulungu.

Dziko lapansi lilibe chimwemwe, chisangalaro kuti munthu akhale nawo ndalama, bizinesi timayenera kudzisaka. Izi zimabweretsa

nkhondo pakati pa maiko zotsatira zake timakhala okhumudwa, amantha, opanda chitetezo, ophana, ziwembu, kutha kwa mabanja, matenda, kuchita zinthu zopanda chipambano,kulephera,matemberero.

Sitinganene kuti ndi mulungu amene akuyambitsa mavuto onse pa dziko lapansi. koma anthu timalephera kupanga chisankho chovomeredza kutsogoleredwa mu Malamulo a chikondi. Nthawi zambiri timatsatira zofuna ndi zikhumbitso zathu kapena boma lathu.

Zaka 6000 zatsala pangono kukwana zimene Mulungu wamphamvu azatenga ulamuliro wonse dziko limeneli ndikubweretsa mtendere.

## KODI IZI ZIZACHITIKA BWANJI?

Pali gulu lokonzekeretsedwa kuchita mwa chipambano pakubweretsa umodz weni weni patatha zaka 6000. Panthawiyi Mulungu adzawonetsa mphamvu zake pamene adzalanda ulamuliro onse ndikubweretsa dziko labwino limene lidzalamuliridwa ndi iye mwini wolenga. Ndipo lidzayendetsedwa mu malamulo a chikondi.

Anthu aku madzulo, mapulofesa, anasakha kukhala ma kominisiti, iwo amati kulibe Mulungu pakuona zinthu zolakwika pa dziko lapansi. Iwo anapitiriza Kunene kuti anali nawo kuthekera, chiyembekezo, chokonza dzikoli kukhala labwino. iwo amanena zowoona koma sanali kufuna kuchita zabwinozo potsatira njira za Mulungu. Iwo amagwiritsa ntchito bodza, malonjezo onama, namatulutsa zotsatira zabodza. Komunisiti chinayamba kuchokera ku maganizo a munthu potsatira chikhalidwe cha munthu ndipo ndi chimodzi mwa chiyembekezo chonyenga.

Koma inu mukhonza kutenga mbali yobweretsa mtendere, chisangalalo, chimwemwe chochuluka kwa anthu amitundu yonse. Mulungu wakonzeka kuchita ichi pogwiritsa ntchito anthu ake pakuwabadwitsa mu chikhalidwe chake amene alapa namalirira pamaso pa Mulungu. pakutero mulungu adzawasintha ndikuwapatsa mphatso yoyera ya chikondi imene idzawapangitsa kuyenda mu chimwemwe, mtendere komanso chisangalalo. Kudzera mu kulapa kwawo ndi chikhulupiriro mwa Ambuye Yesu amakhulupirira kuti adzauka naye mmoyo ndi mphamvu nadzapatsidwa chochita ngati ana a Mulungu nadzalandira chikhalidwe cha uzimu.

Anthu awa adzakhala amene analapa napereka moyo wawo wonse kwa Mulungu kuti iye alamulire mayendedwe awo. (Agalatiya 2:20). nasintha njira yawo imene inabweretsa zopweteka za dzikoli.

Kulapa ndiko kumene kumandipangitsa kukhala khristu weni weni. chiKhristu cheni cheni sikuyankhula za khristu kokha ayi. Baibulo limanena kuti ngati munthu alibe Mzimu wa Khristu siali wake wa Khristu. (Aroma 8:9). Mulungu amapereka Mzimu Woyera kwa onse omvera iye. (Machitidwe atumwi 5:32).

Munthu akalapa sidzimachotsa umunthu umene munthu anabadwa nawo. Maganizo ake amakhala akutsogoleredwa ndi mphamvu ya Mulungu pakulimbana ndi zomusautsa pomukokera mbuyo.

Pakuti onse atsogozedwa ndi Mzimu wa Mulungu amenewo ali ana a Mulungu (Aroma 8:14. Koma kungolandira mziimu woyera sidzokwanira koma munthu wayenera kutsogoleredaw naye. Mzimu

woyera umabweretsa chidziwitso komanso kumvetsetsa kwa choonadi cha mawu a Mulungu. (Mateyu 22: 37- 40, 1 Akorinto2: 10-16, 2 Timoteo 1:7, Aroma 5:5, Agalatiya 5:22). Motero kuti munthu amakhala ndi chikondi cha pa abale onse ndipo amadziwa choyenera kutsata nthawi zonse.

Munthu ayanera kukula ndi chidziwitso cha Mulungu ndi chisomo chake. ( 2 Petro 3:18). Ayenera kukhala ochita malamulo a Mulungu ndikukhala mu mtendere ndi chimwemwe ntawi zonse. Izi sikuthathauza kuti iye ayenera kukhala ogonjetsa chikhalidwe cha Uchimo monga zimene amakonda kale. Khristu ayenera kukhala munthu otsinthika, wachilungamo, wokula m mzimu.

Khristu weni weni amyenera kukhala moyo wophunzira kuti adzalamulire mu ufumu wa Mulungu.

Munthu sangathe kuphunzira mu phindi imodzi, kapena tsiku limodzi, chaka. Kristu sangathe ukhala weni weni pakungomva kamodzi. Timayenera kuphunzira nthawi zonse chifukwa palibe angalondole kuchita zabwino nthwai yomweyo ayi koma amatsata pangono pangono. Ndi chifukwa Baibulo limanena Chibvumbulutso 2:26, 27. Ndipo iye amene alakika ndi amene asunga ntchito zanga kufikira chitsiriziro, kwa iye ndidzamupatsa ulamuliro pa a mitundu.

NDICHIFUKWA CHIANI MAIKO ONSE A DZIKO LAPANSI AYENERA KULAMULIRIDWA NDI KHRISTU NDINSO AMENE APHUNZITSIDWA MOYO WA CHIKHRISTU?.

Njira yokhayo imene ingabweretse mtendere, chuma komanso chimwemwe.

China chili chonse choipa pa dziko lapansi chimabwera kuchokera ku chikhalidwe chathu. Ngati mwayamba njira yoyenera ya Chikhristu musakhumudwe kuti mwatelereka ndi kugwa poyenda mu njira ya Chikhristu. Dzukani ndikuyamba kupitiriza ulendo ngakhale mutachimwa khristu ndi wa nsembe wakutikhululukira ndikumva nafe chisoni. ( 1 John 1:7-10. 2:1-2 ) .

Panthawi yobwera Khristu,onse amene anafa mwa Ambuye adzauka kukawoonana ndi Khristu mulenga lenga. Munthawi yomweyo Akhristu amene analapa adzasinthika mwakanthawi, nadzasiya thupi la pansi pano kulandira la Uzimu la Kumwamba. Iwo adzalamulira pansi pa mphamvu ya Khristu kufikira maiko onse adzataya zida zawo za nkhondo ndipo mtendere ochokera Kumwamba udzaunikira dziko lapansi.

Yesu anawaphunzitsa ophunzira ake kupemphera motere: Kufuna kwanu kuchitike, monga Kumwamba chomwecho pansi pano. (Mateyu 6 :10 ). Motero tayenera kupemphera chimodzi modzi.

# KODI OPULUMUTSIDWA ALONJEZEDWA KUKAKHALA KUMWAMBA NGATI MALO OKHAZIKIKA?

Ndikuti kumene opulumutsidwa adzakhale moyo wawo onse? Kodi inuyo mumakudziwa?

Ndi zoona kuti Mipingo yambiri imene imanena kuti ndi Akhristu imakhulupirira kuti ukalapa udzapita Kumwamba. Timatha kukhulupirira, koma tinayamba tafufuza kuti Baiubulo limati chiani? Kodi Akhristu adzapita Kumwamba ?.

## LONJEZO LA MULUNGU

Pali lonjezo la Mulungu mu Baibulo limene limatiuza zimene opulumutsidwa adzalandire ngati cholowa chawo cha muyaya komanso kumene adzakhale. Lonjezo ili linaperekedwa kwa Akhristu onse. Lonjezo la malo silinaperekedwe kwa akhristu onse koma kwa Abraham. Kupyolera mu lonjezoli Yesu anabadwa kudzera mu mbewu ya Abraham. Pamene munthu atembenuka mtima nakhala wake wa Khristu kupyolera mu lonjezo ili. (Aroma 8: 17 )

Mulungu akunena kudzera mwa Paulo (Agalatiya 3; 16,29. Koma ngati muli a Khristu, muli mbeu ya Abraham komanso Dzizukulu zake kudzera mu lonjezano. Choncho ife tidzalandira cholowa chimene analonjezedwa kholo lathu Abraham. (Aroma 4:11, Agalatiya 3:7,9. Wina aliyense amene amakhulupirira kholo lathu ndi Abraham ali ndi cholowa mu lonjezo la Abraham.

## KHRISTU ANATSIMIKIZA ZA LONJEZOLI

Pofuna kumvetsa za lonjezoli Aroma 15: 8 ikunena kuti; Khristu anakhala mtumiki wa mdulidwe, chifukwa cha choonadi cha Mulungu, kuti akalimbikitse malonjezo opatsidwa kwa Makolo. Yesu anabwera kudzakwaniritsa lonjezo limene linaperekedwa kwa kholo lathu Abraham. (Machitidwe 3: 13, Mulungu wa Abraham, Isaki ndi Yakobo, Mulungu wa makolo athu,analemekeza mwana wake Yesu. Tikapulumutsidwa timalandira lonjezo linalonjezedwa kwa Abraham mu bukhu la Genesis.

### KUMVERA KWA ABRAHAMU

Genesis 12:1. Ndipo Yehova anati kwa Abramu, Tuluka iwe dziko lako ndi kwa abale ako, ndi kunyumba ya Atate ako, kunka ku Dziko limene ndidzakusonyeza iwe.

Mulungu anamuitana Abrahamu kuchoka muzinda umene amakhala poyerekeza Babulo amene tikukhala lero lino. Mulungu akuitana inu ndi ine kuti tituluke Babulo amene tili leroli. Abrahamu sanawiringule ayi ananyamuka kupita ku dziko limene Mulungu anamutsogolera ( ku Palestina). Ngati tifuna kulandira malonjezano a mulungu tayenera kumvera kuti ttilandire malonjezo pamodzi ndi Abrahamu. Tikuyenera kudziwa zimene Mulungu wakonzera omutsatira iye.

1 Akorinto 2: 9. Zimene diso silinaziona ndi khutu silinamva,nisizinalowa mu mtima wa munthu, zimene zili zonse Mulungu anakonzekeratu iwo akumkonda iye. Cholowa chonse chimene Mulungu wakonzekera kwa onse sichingachokere mu maganizo a umunthu.

TISANAYAMBE PHUNZIROLI: Phunziroli

lititthandiza kudziwa choonadi cha mawu a Mulungu. Pamene tikuwerenga tayenera kutsegula bukhu ndi vesi yomwe ngakhale tinayamba tawerenga. Tayenera kulingalira komanso kupemphera kuti Mulungu atipatsa kumvetsetsa kwa phunziroli ndikukhazikika kwa phunziroli mtima mwathu. Phunziroli ndilofunika pa moyo wa Uzimu.

# PHUNZIRO 13: DZIKO LA LONJEZANO.

1. Kodi Mulungu anaitanadi Abrahamu ku Dziko limene amakhala? Genesis 12 : 1. Kodi Mulungu anamulonjeza kumutsogolera pamene ananyamuka ?
2. Kodi Baibulo limanena kuti Abrahamu anawiringula za kuchoka Ku Dziko lake, monga mene ife timawiringula matsiku ano, kuti tikayitanidwa kusiya zoipa zathu timakanika. Abrahamu anamvomera kuchita zimene analamuliridwa kuti anyamuke Genesis 12:4. Mwakutero anapita dziko la Kanani.

NDEMANGA: Kanani ndi Dziko limene matsiku a lero amalitchura Yudeya kapena Palesitina.

3. Kodi nchiyani chimene Mulungu anamulonjeza Abrahamu. ( Genesis 12: 7 ).

Mulungu analonjeza kumupatsa Dziko la Yudeya ku Palesitina ngati cholowa chake ndi mbumba yake. Abrahamu anapita ku Dziko la Eguputo kwa kanthawi.

Kodi atabwerera ku Kanani Mulungu anamuuza kuti apange chiyani, (Genesis 13: 14,15). Kodi Mulungu anabwerezanso lonjezo limene anmupapatsa pamodzi ndi mbeu yake, yonena kuti adzalandira Dziko komanso mbewu yake idzachuluka. (vesi 16).

NDEMANGA: Palesitina ndi Dziko limene Mulungu analonjeza Abrahamu kachiwiri mobwereza. Ichi ndi chifukwa chake limatchedwa Dziko la malonjezo.

4. Kodi Dzikoli Mulungu analonjeza Abrahamu kukhalako matsiku angati?

Cholowacho chinaperekedwa kwa muyaya.

5. Munthu akapatsidwa malo amayenera kudziwa malire a malowo. Nanga malowa anali okula bwanji?. (Genesis 15:18).

Mzindawu unali okula kuposa wa Yudeya.

Tatiyeni tiwone zimene mtumiki Herbert W Armstrong analemba mu bukhu lake:

> Ndipo pamene Abrahamu anali ndi zaka 99 Mulungu anamuonekera nati kwa iye, ine ndine Mulungu wa mphamvu zonse; yenda iwe pamaso panga nukhale wangwiro. Ndipo ndidzapangana pangano ndi iwe. Ndipo ndidzakuchulukitsa iwe kwambiri. Ndipo Abrahamu anagwa nkhope yake pansi. Ndipo Yehova anati pangano langa liri ndi iwe, ndipo udzakhala Atate wa khamu la amitundu onse. Sudzatchedwa Dzina lako Abramu koma Abrahamu chifukwa ndakuyetsa iwe Atate wa khamu la amitundu. (Genesis 17:1-5).
>
> Lonjezo limene linaperekedwa kwa Abrahamu likugwira ntchito mpaka lero. Lonjezoli munthawi yathu labweretsa mafuko ambiri.
>
> Ndipo ndidzakubalitsa iwe ndithu, ndipo ndidzakuyetsa iwe amitundu,ndipo Mafumu adzatuluka mwa iwe.
>
> Ndipo izi sidzikuthathauza kuti ana okhawo osankhikidwa amene anabalalika ayi, koma ngakhale ife amene tinagulidwa ndi mwazi

wake. ( Agalatiya 3:29 )

Koma inu ndinu mbadwa yosankhidwa. Ansembe achifumu,mtundu woyera,anthu a mwini wake,kotero kuti mukalalikire zoposa za iye amene anakuitanani mutuluke mu mdima,mulowe mu kuunika kwake kodabwitsa. ( 1 Petro 2:9 ). Choncho Mpingo wa Khristu sunagawikane pokamba za mitundu tili amodzi mwa chisomo chake.

Ndipo ndidzalimbikitsa pangano langa,ine ndi iwe pa mbewu zako za pambuyo pako,Mibadwo yawo kuti likhale pangano la nthawi zonse. ( Genesis 17:7,8,9 )

Mtsogoleri Herbert A Armstrong anawona china chosangalatsa pa lonjezo la Mulungu kwa Abrahamu.

Genesis 12:1-3. Ndidzakudalitsa iwe ndikubukitsa Dzina lako,nukhale iwe Mdalitso, ndidzadalitsa iwo akudalitsa iwe,ndikutemberera akutemberera iwe,mwa iwe adzadalitsidwa mabanja onse a Dziko lapansi.

Lomweli tili kulipedzanso pa Genesis 22:18. Ndi Agalatiya 3: 8,16

Genesis 49:10. Ndodo ya Chifumu sizachoka mwa Yuda,kapena wolamulira pakati pa mapazi ake,kufikira atadza silo,ndipo anthu adzamvera iye.

1 Mbiri 5: 2. Pakuti yuda anakula mphamvu mwa abale ake,ndi Mtsogoleri anafuma kwa iyeyu, koma ukulu ngwa Yosefe.

Zoonadi zake apa ndizoti ndodo ya chifumu inapita kwa Yuda, ndi chifukwa chake Mfumu Davide anali wa pfuko la Yuda. Onse analowa Ufumu wa Davide anali a mnyumba ya Davide pfuko la Yuda. Ambuye Yesu anabadwa mu pfuko la Yuda, kunyumba ya Davide.

5. Mulungu anapereka malonjezo kwa Abrahamu okhuza uk uzimu ndi kuthupi, lonjezo la kuthupi silinakwaniritsidwe pa Ayuda komano akukwaniritsidwa matsiku ano otsiriza. (Genesis 28:13,14. Mateyu 5:5. Masalimo 25:13, Aroma 4:13, Genesis 28: 13,14.)

## TIYENERA KUMVERA TISANALANDIRE CHOLOWA CHA UFUMUWO

Lonjezo la cholowa cha Mulungu kwa Abraham linakhazikitsa pa iye pamene iye anamvera kuyankhula kwa mulungu. Abraham anasiya Dziko lake, ana, mabwenzi komanso njira zakake zimene anali kuchita. Mulungu atamuitana Abraham sanalekere pompo koma anapitirira kumuuza zoti achite

1. KODI MULUNGU ANAMUYETSA ABRAHAMU MOTANI

Genesis 22:1,2. Mulungu anamuyesa Abrahamu nati kwa iye, Abrahamu nati ndine pano.ndipo anati tenga Mwana wako wa Mwamuna yekhayo Isaki amene ukondana naye nupite ku dziko la Moriya numpereke iye nsembe yopsereza.

NDEMANGA: Mulungu sayesa munthu ndi cholinga choti akagwe, koma kuti akaona kumvera ndi kudalilika kwa munthu.

2. Kodi Abrahamu atamva mawu awa anawiringula kapena kupereka zifukwa, kuukira,ndikuthawa? Choonadi pa nkhaniyi ndi choti iye anamvera Mulungu ndi mtima wonse nadzuka mamawa kupita kukapereka nsembe.

3. Kodi Abraham anmutengadi mwana wakeyo?. (Genesis 22:10-12.) Mulungu sanamutenge isaki koma amangofuna kuona kumvera mwa Abrahamu. Chifukwa Abrahamu anakhulupirika, anali wodzala ndi chikhulupiriro baibulo limamunena kuti tate wa chikhulupiriro.

4. Atamvera Abrahamu pakuyesedwa anapambana ndipo Mulungu anati kwa iye . Genesis 22:15 -18. M"mbewu zako mitundu yonse ya Dziko lapansi idzadalitsidwa chifukwa wamvera mawu anga.

NDEMANGA: Lonjezoli linali la muyaya .

5. Kodi Abrahamu mokhulupirika anali kumvera Mulungu mu njira ina iliyonse. ( Genesis 26:5 )

Malamulo amene Adamu anawaphwanya pa chiyambi ndi malamulo omwewo Abrahamu anawamvera, nawasunga. ( 1 Yohane 3:4 )

6. Lonjezoli linapitirira kugwira ntchito pa mwana wake Isake,motero mitundu yonse ya Dziko lapansi imadalitsika kudzera mwa Isake. ( Genesis 26: 1-5 )

7. Lonjezoli likupitirira kuonekanso pa Yakobo amene ndi mwana wa Isake . ( Genesis 35: 9-12 )

Yakobo amene dzina lake linasinthidwa kukhala Israeli ( Genesis 32:8 ) anali ndi ana 12 . Mwana aliyense anapanga pfuko limodzi la Israeli.Kudzera mwa Khristu chipulumutso chinaperekedwa kwa Ayuda (YOHANE 4:22, Aroma 2:11-12 ). Anthu onse pa dziko lapansi amene sanabadwa kudzera mwa pfuko la Abrahamu baibulo limawatchula kuti ndi amitundu.

8. Lonjezano linaperekedwa kwa Abrahamu, Isake,Yakobo ndi ana a Yakobo,ndipo ana a Yakobo ndi amene ali ma Israeli osati amitundu ( Aroma 9: 4-5 ).

## AKHRISTU OKHULUPIRIRA NDIWO ENI MALONJEZO

Popeza malonjezano anaperekedwa kwa Abrahamu ndi mbewu yake, nanga ndi chifukwa chiani Maiko onse ali nawo malonjezowa.

1. Kodi Mulungu anapereka malonjezo kwa Abrahamu kuti mitundu yonse yokhala Dziko lapansi ikadalitsidwe kupyolera ku Mbewu imodzi. (Genesis 12: 3, Genesis 22: 18 ). Nanga mbewu iyi ndi ndani? (Agalatiya 3:8,16 ). Mbewuyo ndi Abrahamu monga mwa malembo. (Genesis 13:16, 17:8 )

2. Luka 3:23,24 limatsimikiza kuti Yesu anachokera mu mbewu ya Abrahamu. Maria make a Yesu anachokera mu pfuko la Abrahamu kudzera mwa bamboo wawo Eli. Ngati mufuna kudziwa zambiri werengani bukhu lotchedwa NDICHIFUKWA CHIANI YESU ANALI NDI MITUNDU IWIRI? Kudzera pa webusite yathu: (www.cogwriter.com)

3. Kodi Paulo adafotokoza zotani zukhuza amitundu kuti alandire nawo malonjezano amene anaperekedwa kwa Abrahamu? Genesis 3:26-29.

Ayenera kubatizidwa mwa uzimu kudzera mwa Yesu khristu ndiponso ubadwe mwatsopano.

4. Paulo anawauza akhristu aku Aefeso kuti kale munali opanda chiyembekezo ngakhale pangano la Mulungu asanatembenuke mtima, koma pamene anatembenuka ndiwo Aisraeli kupyolera mwa Khristu.

5. Koma tsopano kupyolera mwa Khristu yesu ali pafupi naye. Aefeso 2:13.

Aliyense ovomeleza kuchokera ku mafuko osiyanasiyana athe kubwera kwa iye namwe madzi a moyo kwaulere chifukwa Mulungu wasunga lonjezo lake ndi mbewu ya lonjezo mwa Khristu Yesu amene ali palate pa onse.

Aroma 8:14-15. Pakuti onse otsogozedwa ndi mzimu wa Mulungu ali ana a Mulungu. Mzimu umene umatipangitsa kufuula kuti Abba Atate.

Ufumu wa Mulungu ndi banja la mulungu lodzala ndi ulemerero umene uposa chilichonse.

Kma kusiyana kwake ndi kotani pa kulandira dziko lapansi ndi kulandira ufumu wa Mulungu? kodi ufumu wa Mulungu tidzaulamulira kuti?

## PALIBE MUNTHU ADAKWERA KUPITA KUMWAMBA, NDI YESU YEKHA BASI.

Baibulo limanena kuti dziko lapansi ndi cholowa cha anthu opulumutsidwa osati kumwamba.

1. Yesu anayankhula kuti palibe anapita kumwamba. Yohane 3:13

   amene ali kumwamba amene akuyimbira mulungu, Chibvumbulutso 5:11-12.

   Bukhu lina limene limawasokoneza anthu ndi Afilipi 3:20. Pakuti ufulu wathu uli kumwamba, kuchokera komweko, tilindira Mpulumutsi Ambuye Yesu Khristu.

Anthu olalalikira akhala akulakwitsa pomatsulirira bukhuli.

Pa Chigiriki mawu oti ufulu amatchedwa LOGOI, monga mene anenera pa Luka 24:17. pamene pothathauzira ku Afilipi mawu oti ufulu anawatcha kuti POLITEUMA.

Choncho ufumu umene tili kuyembekezera pa dziko lapansi uli kumwamba,ndipo tiyembekezera Khristu kudzabwera.

Chifukwa Yerusalemu watsopano abwera kuchokera kumwamba (Chibvumbulutso 21:) ndipo ife sitiri a dziko lapansi monga malembo a pa Yohane 15:19 koma Ufumu wathu uli Kumwamba.

Kumwamba sikwathu chifukwa ife tonse Akhristu tinasandulika kukhala anthu a Mulungu.

1 Petro 2:9-10. Koma inu ndinu mbadwa yosankhika, Ansembe achifumu, Mtundu woyera mtima, Anthu a mwini wake, kotero kuti mukalalikire zoposazo za iye amene anakuitanani mutuluke mu mdima mulowe mu kuunika kwake kodabwitsa. Inu ameme kale simunali anthu, koma tsopano muli anthu a Mulungu, amene kale simunalandira chifundo, koma tsopano mwalandira chifundo.

Popeza Ufumu wathu uli Kumwamba panopa. choncho ulamuliro wathu panopa uli Kumwambanso kufikira atabwera Khristu.

NANGA MOSE NDI ELIYA?

> Mateyu 17 :1–9. Pamene Yesu ananenapo za Petro, Yakobo ndi Yohane pamene anapita Paphiri lalitari ndipo Mose, Eliya anawaonekera iwo ali kuyankhula ndi Yesu.

## KUKWANIRITSIDWA KWA MALONJEZANOWO OMWE ALI PATSOGOLO

Kodi Abrahamu watha kulandira malonjezowo? Choyamba taityeni tiwone baibulo za STEFANO poyamba kuphedwa, amene anali odzala ndi chikhulupiriro ndi Mzimu woyera. Ndipo iye anapereka moyo wake chifukwa cha mawu a Mulumgu.

1. Kodi Abrahamu adalandiriratu cholowa chimene Mulungu anamulonjeza? (Machitidwe atumwi 7:2-5) makamaka vesi 5. Ndipo sanamupatsa cholowa chake mmenemo ngakhale popondapo phazi lake. Ndipo anamulonjezera iye kuti adzamupatsa ili likhale lake

NDEMANGA; Abrahamu sanalandire lonjezo la cholowacho ngakhale lonjezo la Mulungu linalipo, iye anangomunikiritsa chifukwa iye anamvera Mulungu.

2. Kodi Abrahamu anangokhala mlendo mu dzkiko limene Mulungu anmulonjeza?

Ahebri 11:8-10. Ndi chikhullupiriro anakhala mlendo ku dziko la lonjezano,losati lake,nakhalira mmahema pamodzi pamodzi ndi Isake ndi Yakobo, olowa nyumba pamodzi ndi iye alonjezano lomwelo.

Kodi ngakhale iye anamwalira anali atalandira malonjezanowo. Ahebri 11:13, Iwo onse adamwalira mu chikhulupiriro, koma osalandira malonjezano, komatu adawaona ndi kuwalankhula kutali, navomereza kuti ali alendo ndi ogonera pa Dziko.

Kodi vesi 8 ikutsonyeza kuti Abrahamu adzalandira mtsogolo malonjezanowa?

3. Kodi limafokoza kuti Isake ndi Yakobo anali nawo mbali pa malonjezanowa? ( Ahebri 11:9 ).

NDEMANGA: Kodi mukutha kumvetsa malembawa chimene Mulungu akuyankhula. Malemba akunena kuti onse atamwalira, panatha zaka chikwi lonjezoli lisanalembedwe.

4. Kodi Abrahamu anali atafa mu nthawi ya Atumwi. Yohane 8:52,53.

Koma ndi chifukwa Abrahamu mpaka pano sanalandire cholowa cha panganolo?. Khristu anabwera kudzakwaniritsa za lonjezo lakuti dziko lapansi linalonjezedwa kukhala cholowa cha Abrahamu.

Posachedwa Abrahamu adzabadwa mu ufumu wa Mulungu, popeza ndife mbewu ya Abrahamu tidzalandira cholowa cha Ufumuwo kudzera mwa Khristu.

## MALANDIRIDWE A UFUMU WA MULUNGU.

1. Mateyu 6:33. Imatsimikiza kuti tiyenera kufunafuna Ufumu wake osati Kumwamba ayi.
2. Mateyu 7:21. Ikunena kuti siwonse anena kuti Ambuye Ambuye adzalomwe mu Ufumu wake, koma wakuchita chifuniro chake.
3. Bukhu la Aefeso 5:5 limanena kuti wosapulumutsidwa sadzapezeka mu Ufumu Mulungu popeza Ufumuwo ndi wa okhawo amene analapa.
4. Ambuye Yesu ananena kuti Ufumuwo suli wa Dziko lapansi. (Luka 2:31, Yohane 18:36). Ufumu wa Mulungu ndi umene udzalamulire dziko lapansi ndipo uli pafupi.

5. Kodi Ufumu wa Mulungu wakhazikika kale pa Dziko lapansi. Choonadi ndi choti Ufumu wa Mulungu sunakhazikike pa Dziko lapansi. (Luka 19:11-13,15)

6. Yesu anawauza ophunzira ake kuti apemphere kuti Ufumu wake udze. (Mateyu 6:9,10).

Yesu anawatumiza ophunzira ake kupita kukalalikira za Ufumu wa Mulungu. (Luka 9: 1,2 Mateyu 12: 28).

Ufumu weni weni uli mtsogolo osati panopa.

> Marko 9:47. Ndipo ngati diso lako likuchimwitsa kuli kwabwino ulikolowe,ndinkwabwino kukulowa kumwamba uli ndi diso limodzi koposa maso awiri ndikuponyedwa ku Gehena.
>
> Marko 10: 23-25. NdipoYesu anaunguza unguza nanena ndikovuta kuti wachuma akalowemu Ufumu wa Mulungu. Ndikwapafupi kuti ngamila ipyole diso la singano koposa kuti mwini chuma akalowe mu Ufumu wa Mulungu.
>
> Marko 14:25. Ndinena nanu, simudzamwanso chipatso cha Mpesa kufikira tsiku lijalo, limene ndidzamwa icho chatsopano mu Ufumu wa Mulungu.
>
> Marko 15;43. Yosefe wa ku Arimateya anali kuyembekezera Ufumu wa Mulungu.

7. Ndondomeko za onse oyera mtima kulandira Ufumu wa Mulungu zikusungidwa Kumwamba. (1 Petro 1:3,4,5. Ichi ndi chitsimikizo kuti Ufumu wake sunafike panopa koma tikuyembekezera kubwera kwa Ambuye posachedwapa.

8. Sitingalandire Ufumuwo popeza tiri a thupi ndi mwazi. ( Akorinto 15: 50 )

NDEMANGA; Thupi ndi mwazi sidzingalandire ufumu wa Mulungu. Chotero matupi athu adzasanthulika mwa uzimu kuti akathe kulandira nawo Ufumuwo. (Chibvumbulutso 20:4-6).

9. Paulo akunena kuti matupi athu adzasintha, (1 Akorinto 15: 51,53)

Popeza tidzabadwa mwa uzimu nanga matupi athu adzaoneka motani? (Yohane 3:3-6 ).

10. Kodi zizatenga nthawi yotalika bwanji kuti matupi athu asinthike kukhala a Uzimu. 1 Akorinto15:52 Mukamphindi,kuthwanima kwa diso pa lipenga lotsiriza.

## OPULUMUTSIDWA PA TSIKU LA KUUKA KWA AKUFA

Sitingathe kulowa mu Ufumu wa muyaya tisanayambe kulowa mu moyo wa muyaya popeza tayenera kukhala ndi chiyembekezo chodzauka kwa akufa.( Ahebri 9:27. Kwaikidwa kwa Munthu kufa kamodzi).

1. Ngati kulibe kuuka kwa akufa ,Khristu sanaukitsidwe, (1 Akorinto 15:13. )

2. Ngati Khristu sanaukitsidwe kulalikira kwathu ndi kwachabe, (1 Akorinto 15:14). Chifukwa chake iwo akugona mwa Khristu anatayika vesi 8. Ndichifukwa pali kuuka kwa akufa kuti amene anatayika monga Abrahamu, Isake ndi Yakobonawo aukitsidwe.

3. Yesu ananena kuti kuuka kwa akufa kudzachitika kwa onse anamwalira ali mu chipulumutso. ( Mateyu 22:31,32 ).

## KODI KHRISTU ANAPANGA BWANJI KUTI CHOLOWA CHATHU CHITHEKE?

1. Kodi tchimo ndi chiani? 1 Yohane 3:4 Nanga mphoto yake ndi chiyani? Aroma 6:23 Kodi onse anachimwa? Aroma 3:23

Iye amene samvera Mulungu amakhala ochimwa ndipo amafa kwa muyaya.

2. Khristu Yesu anakhetsa mwazi wake malo mwathu kudzera ku chiombolo cha machimo athu. ( 1 Timoteo 2:5. Aroma 5: 8-10 ).

Iye anasandulika thupi ( Yohane 1: 14 ). Mulungu atate analenga chili chonse pamodzi ndi Yesu Khristu ( Aefeso 3:9. Yohane1:1¬-3 )

3. Khristu anapereka pangano. (Ahebri 9:15-17. Ahebri 1: 14 )

## TINGACHITE CHIANI KUTI TILOWE MU MALONJEZANOWA

1. Tiyenera kukhulupirira Khristu. (Yohane 3:16, Aefeso 3: 4 -6, Agalatiya 3: 9)
2. Tiyenera kudziwa kuti Khristu anadzipereka nsembe malo mwathu. (Luka 22:42,44. Yesaya 52: 14.)
3. Kuzunzika kwa Khristu ndi imfa ya Khristu zinatipanga ife kukhala afulu kutumikira iye. 1 Akorinto 7:23. Ngakhale ena akumukana kuti iye sanawagula ndi mwazi (Malaki 3: 14, 2 Petro2:1).
4. Tiyenera kumvera ndi kusunga malamulo ake monga mene Abrahamu anachitira, Mateyu 19: 17, Genesis 26: 5.).
5. Paulo pa utumiki wake amanena kuti chili chonse chimene amachita chimachokera kwa Mulungu. (Akolose2:22-24, Machitidwe atumwi 27:23).
6. Tiyenera kumvera nthawi zonse. (2 Akorinto 2:9, 2 Akorinto10:5)
7. Kumvera kumatithandiza kuchita choyenera nthawi zonse ( Aroma 7 :7,12 ).

## TIDZALANDIRA MALONJEZANO KHRISTU AKADZABWERA

1. Kodi Abrahamu ndi ana ake adzalandira malonjezo kudzera mwa Khristu liti ? ( Pa lipenga lotsiriza. 1 Akorinto 15: 52,53.
2. Akadzabwera Khristu ife otsala ndi moyo tidzakwatulidwa nawo pamodzi mu mitambo. ( 1 Atesalonika 4:16,17. )
3. Ndipo patsikuli Yehova adzakhala iye Mfumu ya Dziko lapansi ( Zekariya 14;9-10)

Pa lipenga lotsiriza,Khristu adzabwera ku Dziko lapansi ngati Mfumu ya Mfumu,Mbuye wa Mbuye. Ndipo Abrahamu ndi mbewu yake adzalandira cholowa chawo.

## LONJEZO SILINENA ZA KUMWAMBA

Yesu anati Odala ali akufatsa chifukwa adzalandira Dziko lapansi, ( Mateyu 5:5 ).


Kulibe munthu anakwera kumwamba,koma iye wotsika kumwamba ndiye mwana wa munthu, wokhala mwambayo. ( Yohane 3: 13).

1. Pakuti iwo akuyembekezera Yehova adzalandira Dziko lapansi. Masalimo 37:9,

2. Adzadalitsidwa vesi 22.
3. Adzalandira Dziko lapansinadzakhala momwemo kosatha vesi 29.
4. Yembekezera Yehova nusunge njira yake, ndipo iye adzakukweza kuti ulandire Dziko, Pakudulidwa oipa udzapenya. ( Masalimo 37:34 )

NDEMANGA: Palibe mawu mu baibulo amene amanena kuti Mulungu analonjeza kuti opulumutsidwa mwa Khristu adzakhala kumwamba, ( Mateyu 25:31,34. )

# KODI CHIPANGANO CHAKALE CHIMAPHUNZITSA ZA UFUMU WA MULUNGU?




**Wolemba ndi: Bob Thiel**

Kodi ana Aisraeli amadziwa za Ufumu wa Mulungu kudzera nu malemba a chihebri?

Baibulo limanena kuti ma uthenga amene Yesu amalalikikira amakhunza za Ufumu wa Mulungu, Marko1: 14¬-15, Machitidwe atumwi 1:3 ). Ufumu wa Mulungu chinali chiphunzitso chimene Ayuda amachidziwa mu nthawi ya Yesu.

## DANIELI ANAYANKHULA ZA UFUMU

Neneri Danieli analemba: Ndi Ufumu wa chinayi udzakhala olimba ngati chitsulo, popeza chtsulo chiphwanya ndi kufooketsa zonse,ndipo uwu udzaphwanya zonse. Ndipo matsiku a Maufumu aja, Mulungu wa kumwamba adzaika Ufumu oti sudzaononongeka ku nthawi zonse, ndipo ulamuliro wake sudzasiyiridwira mtundu wina wa anthu. ( Danieli 2:40-44 )

> Danieli 7: 18. Koma wopatulika a wamwambamwamba adzalandira Ufumuwo ndikukhala nawo Ufumuwo kosatha,kunthawi zomka muyaya.21. Ndinapenya, koma nyanga yomweyi inachita nkhondo ndi opatulikawo niwalaka mpaka inadza nkhalamba ya kale lomwe22 Ndipo mlandu unakomera opatulika a wamwambamwamba,Nifika nthawi yoti Ufumu unali wao wa opatulikawo.

Kuchokera mwa Danieli timaphunzira kuti nthawi ikubwera imene Ufumu wa Mulungu udzaononga ma Ufumu a Dziko lapansi kwamuyaya.

Chibvumbulutso 17:12 -14.

Muchipangano cakale ndi chatsopano chikutsimikiza kuti Mulungu adzaononga ma ufumu onse a Dziko lapansi, nadzakhazikitsa Ufumu wake.

# YESAYA ANAYANKHULA ZA UFUMU

Yesaya analembapo za gawo loyamba la Ufumu wa Mulungu. (Yesaya 11: 1-10 ) Ufumu wa mtendere wa Mesiya udzakhazikika, Ndipo Dziko lapansi lidzazala ndi odziwa ndi kuopa Mulungu. Ndipo sadzaweruza monga apenya maso, nadzakondwera nawo kuopa Yehova.

> Pakuti Yerusalemu watsopano akudza kuchokera kumwamba (Chibvumbulutso 21:) ndipo adzakhala kwa chaka chikwi.
>
> Yesaya akupitiliza kunena kuti patsikulo Ambuye adzabwera kachiwiri ndipo amene anabvuta Yuda adzadulidwa. (Yesaya 11: 11-16).
>
> Bukhu la Yesaya 2: 2-4,11. Liri kunena za Ulemerero wa Israyeli mutsogolomo.
>
> Udzakhala mtendere wa Dziko lapansi ndi Yesu akulamulira. (Masalimo 90:4, 92: 1, Yesaya 2:11, Hoseya 6:2 .

Yesaya anauzidwanso kulemba za choneneratu cha Ufumu wa Mesiya. (Yesaya 9:6-7). Yesaya ananena kuti Yesu adzabwera nakhazikitsa Boma ndi malamulo ake, ndipo Yesu adzakhala pamwamba pa Malamulo. Pakuti Malamulo a Mulungu ndi njira ya Chikondi (Mateyu 22:37 -40. Yohane15:10). Ndipo Ufumu wa Mulungu udzatsogolera molingana ndi Malamulowo.

EZEKIELI NDI MASALIMO ANAYANKHULAPO ZA UFUMU WA MULUNGU

(Ezekieli 11:17- 21)

Pfuko la Mtundu wa Israeli sudzamwazikana koma udzamvera Malamulo a Mulungu ndikusiya kudya zinthu zodetsedwa ( Levitiko 11: Deutoronomo 14: )


Tiyeni tione bukhu la Masalimo az Uthenga wabwino okhudza Ufumu wa Mulungu.

1. Masalimo 22: 27,28.
2 Masalimo 45:6. Mpando wa Ufumu wanu ukhala nthawi zonse zomka muyaya.
3. 1 Mbiri 16: 23,24. Muyimbireni Yehova ,inu Dziko lonse lapansi. Lalikirani chipulumutso chake tsiku ndi tsiku. Fotokozerani ulemerero wake mwa amitundu . ( Masalimo 96; 1-3 )
4. Masalimo 145: 10-13. Ntchito zanu zonse zidzakuyamikani Yehova, ndi okondedwa anu adzakulemekezani.Adzanenera ulemerero wa Ufumu wanu. Adzalakhula za mphamvu yanu.

NDEMANGA: Olemba ambiri analembapo zokhudza Ufumu wa Mulungu monga Obadiya 20:, Mika 4:7, Ezekieli 20:33.

Yesu pamene anayamba kuphunzitsa za Ufumu wa Mulungu sikunawavute amena anamumva koyamba kudzindikira ichi.

# SITIDZATHAWA CHITSAUTSO CHA CHIKULUCHO



Ngamila ku Petra

**Wolemba: LEROY NEFF**

Nkhaniyi inalembedwa ndi Old Radio Church of God mu January 1962.

PETRA ndi malo amene akhristu a ku Feladefiya amakhulupirira kuti azapulumukirapo pa nthawi ya chitsautso chachikulu.

Yesu ananenapo pa nkhaniyi: Luka 21:36. Koma inu dikirani nyengo zonse ndi kupemphera kuti mukalimbike kupulumuka zonse zimene zidzachitika, ndikuimirira pamaso pa mwana wa munthu.

Tikuudzidwa kuti tiyenera kupemphera nthawi zonse, tsiku liri lonse kuti tidzathe kupulumuka ku zonse zimene zidzachitike koma timalephera udindo wathu kuuchita.

## UNENERI WODABWITSA MATSIKU ANO

Kupulumutsidwa kwa Mpingo wa Mulungu,kubwera kwa Yesu Khristu zanenedwa mu bukhu la Chibvumbulutso 21:

Munthawiyi yathu ino Satana ali pa ukali ndi anthu a Mulungu chifukwa akudziwa kuti nthawi yamutsalira pangono kuti anamize Dzikoli. Pakutero adzapitiriza kunzunza mopitiriza muyeso koma Mulungu adzatitetedzera mpaka tikafike malo a mtendere chisanafike chisautso chachikulu.

> Chibvumbulutso 12:14. Ndipo anamupatsa mkazi mapiko awiri a chiombankhanga chachikulu kuti akaulukire ku chipululu, kumbuto yake, kumene adyetsedwako nthawi ndi nthawi, osapenya nkhope ya njoka.

Simpingo wonse wa Mulungu umene udzapite ku mtenderewo, koma amene anatenga mbali yawo mu ntchito ya Mulungu adzatengedwa kupita.

> Otsalawo adzakhala amene anasunga malamulo komanso umbonu wa Yesu Khristu koma sanayenere kupulumuka. Ndipo Satana adzachita Nkhondo Ndi anthu awa. (Chibvumbulutso 3: 10 -12)

Tiyenera kuonetsetsa kuti Mayitanidwe athu akhale oyenera chifukwa tikhoza kukhala mumpingo wa Mulungu koma osakhala mu choonadi cha Mawu a Mulungu.

Anthu amene abatidzidwa mu mpingo wa Mulungu amapita ku msonkhano wa misasa (Feast of Tabernacle chaka ndi chaka, ndipo ena amalephera chifukwa cha Matenda, Chuma, Banja lawo linawakanitsa kupita, Choncho ife amene timapita kodi sitili ngati Aisraeli amene amangokhalira kung'unguza, sanali kumvera Mulungu ngakhale Utsogoleri wa Mpingo.

KODI MULI NDI ZOLINGALIRA ZOLAKWIKWA?

Ambiri tili ndi malingaliro olakwikwa koma sitimadziwa. Tikuyembekezera kudzapulumuka ku chisautso cili kudza pamene tikutsatira zikhulupiriro za bodza zimene zipembedzo zambiri zimaphunzitsa matsiku ano.

Mipingo ina imanena kuti MKWATULO ndi njira yokhayo imene idzatipangitsa kuzemba Gehena.

Tiyenera kumvetsa bwino zimene zinaloseledwa zokhuza malo a mtendere amene Mpingo wa Mulungu udzapite.

Idzakhala nthawi ya masautso akulu,nkhondo, njala, zimene sidzinachitikepo. (Mateyu 24:) Imene iwo amene adzakhale mu Yudeya akulamuliridwa kuthawira ku mapiri. Idzakhala nthawi imene munthu sadzakwanitsa kulowa nyumba yake kuti atenge zovala ndi zinthu zake. Azimayi amene adzakhale ndi pakati komanso ana oyamwa azakhala pa mavuto akulu. (Chibvumbulutso 12:15,16.)

## PARADIZO KAPENA CHIPULULU

Panthawiyi ena sadzakwanitsa kupirira mpaka atangonjetsa chitsautsochi, Ndi okhawo okhulupirira a mu Mpingo wa Mulungu amene adzapulumuka mu nyengoyi. (Chibvumbulutso 12:14)

Danieli 11:41. Adzalowanso mu Dziko lokometseysalo, ndi maiko ambiri adzapasuka; koma opulumuka dzanja lake ndi awa Edomu, Moabu, ndi ana oyamba a Amoni.

Kumene anthu adzathawire adzakhala malo Otetedzedwa otchedwa PETRA. Mawu oti Petra ndi chigriki pamene mu chiheberi amatchedwa SELA. (Yesaya 42: 1. 6: 1-5. Masalimo 108: 10. )

Iwo amene adzayenera kupulumuka pa chisautsochi adzatengedwa kupita ku PETRA. Petra ndi malo amene ngakhale ndege sidzinafikeko. Ndi Mulungu amene akudziwa njira imene adzagwiritse kuti tidzakafike ku malowa ngati tidzayetsedwe oyenera.

## WODANDAULA SADZAPULUMUKA PA NTHAWIYI

Matsiku ano timadandaula tikasowa chakudya, ndalama,madzi, malo ogona, utsogoleri umene Mulungu anasankha, . Choncho ngati tili ndi malingaliro otere sitingapezeke ku Petra

## KODI PETRA ILI MOTANI

Magazini otchedwa National Geographic Magazine mu Febuluare 1935, komanso Desembala 1955. Ngakhale mayi Herbert Armstrong analemba za Petra.

Petra ndi malo okongola, ali ndi Phanga,Madzi abwino, kumene Mpingo wa Mulungu udzapita kukatetedzedwako.

## PHUNZIRO LIMENE TIYENERA KUPHUNZIRA

Luka 21:34-36. Ndipo mudziyanganire nokha kuti kapena mitima yanu ingalemetsedwe ndi zosamalira za moyo uno, ndi kuti tsikulo lingakufikireni modzidzimutsa ngati msampha.

Pakuti lidzatero ndikufikira anthu onse akukhala pa nkhope ya Dziko lapansi. Koma inu dikirani nyengo zonse ndi kupemphera, kuti mukalimbike kupulumuka zonse zimene zidzachitika ndi kuimirira pamaso pa mwana wa munthu.

Lamulo likuti Yanganirani ndi kupemphera nthawi zonse Mateyu 6: 9-13. Tikapemphera mokhulupirika ndi mtima wathu wonse tidzakwanitsa kupulumuka pa nthawiyi.

Sitiyenera kupemphera kuti tipulumuke kokha ayi komanso kubwera kwa Yesu Khristu.

Deuteronomo 28:47, 48. Popeza simunatumikire Yehova Mulungu wanu ndi chimwemwe ndi mokondwera mtima, chifukwa cha kuchuruka zinthu zonse. Chifukwa chake mudzatumikira adani anu amene Yehova adzakutumidzirani ndi njala, ludzu, usiwa, kosowa zonse, ndipo adzaika goli la chitsulo pakhosi lanu, kufikira atakuononongani.

Ichi ndi chifukwa chimene anthu osankhidwa ndi mulungu sadzapita kumalowa chifukwa sakutumikira Mulungu ndi chimwemwe ndi mtima wonse.

Malo moyamika Mulungu timadandaula tikaona ena zikuwayendera panene izi zingatilepheretse kupita ku petra. Tiyenera kudziwa kuti mavuto amene timakumana nawo ndi ochepa kuyerekeza ndi amene akubwera.

Tiyeni tigwiritse nthawi imene tili nawo kuti tikule mu uzimu umene udzatithandize kugonjetsa mayesero amene akubwera kutsogoloku. Madalitso amene tili nawo tiyeni timuyamika nawo Mulungu posadera nkhawa pa zochitika za dziko lapansi.

Tiyeni tiphunzire kupemphera tsiku ndi tsiku komanso mene tingagonjetsere mayesero amene tikukumana nawo matsiku a moyo wathu.

LANGIZO LOMALIZA

1 Akorinto 10: 1-13 Paulo mtumwi akunena kuti zonse zimene zinalembedwa mu nthawi yakale zinalembedwa kuti dzitiphunzitse ndi kutilangiza. Ngati sitingatero sitidzapulumuka ayi.

Abale, Mulungu adzapereka njira yopulumukira, idzakhala yovuta koma ndiyo njira ya chimwemwe.

KODI MUDZAKHALA MODZI WA OTETEDZEDWA NDI KUIMA PAMASO PA YESU KHRISTU AKADZABWERA?

# Baptisms in Malawi and Mozambique

**Evangelist Evans Ochieng sent in the following report related to his trip to Malawi and Mozambique:**

Greetings from Malawi.

I was very happy when counseling these people. Among them were some old ladies and men whom I thought have learned nothing. But this people were deep in truth and they new the reason why they are need of baptism. I appreciated the work we have been doing in Malawi and the work which our brother Grantone Otieno did during the Feast Of Tabernacles 2017. Grantone did a wonderful work to put all the teachings in place. He touched all the subjects during his days in the Feast of Tabernacles.

I want to appreciate the great work our brother Mulozowa has done in both Malawi and Mozambique with in few years that we choose him to our representative in Malawi. This man has done a wonderful work with a good plan of work. May God bless him for his work.

With the 2 hours of our meeting in Mulozowa's home, I touched Many subjects and true repentance. One of the attendees decided the next Day not to go for her baptism. Plus another girl was still young but she wanted to be baptized. I did counseling to her and she noticed the real meaning of baptism and its importance. Since she was still school girl, she decided to wait and not to be baptized at this moment. This girl is a wonderful girl. Her parents did not want her to keep sabbath while the whole family are keeping Sunday. So they chased her out of their home if she has decided to join Continuing Church of God. But the girl accepted our teachings and moved out of their home simply because she wanted to follow the truth. So this girl is now in Mulozowa's home. I am still thinking how we can assist this girl and if there is a way how we can assist her to continue with her school will be great.

On Friday we took a bus to Mozambique very early in the morning. When we reached at the border I found Mulozowa had already made things good I was not disturbed to go in Mozambique. We went early because I wanted to meet the brethren in Mozambique who wanted the baptism. I took two hours counseling them.

## MOZAMBIQUE

I met very many people from Mozambique who wanted to be baptized. I took almost three hours when I was counseling them. Among them was a man who divorced his wife. I took time to talk with him about marriage and the reason why God hates divorce (Malachi 2:15-16) After a long discussion the man decided himself not be baptized till he go back to his wife and talk with her. He said that he is going to take Mulozowa

and Matiya to the lady's home so that they can talk with her deeply about the word of God.

"The total number of members who were baptized were 34. 16 members from Malawi and 18 members from Mozambique. Since I became a pastor, this is the largest work of baptism that I have done in my life. Even though it was a big work and tough, it was done perfectly and I thank those who prayed for me during my trip to Malawi. The Baptism was done in a river called Chirewe in Mozambique. it is a big river with plenty of water.I appropriate the joint hands of Mulozowa and Matiya. The rest of members were not baptized because the were still learning. And I want to inform you pastor that the doors are open in Malawi and Mozambique. I did not expect the extent of the work I have seen in Malawi. Let us pray for the work in Africa.

On the Sabbath we met in Malawi. Our brethren from Mozambique came to Malawi. Even though I was but one person, I touched many subjects. The importance of Christian calling and our major work, true repentance, divorce and remarriage, tithing, and the Sabbath.

The Sabbath was wonderful. The number was 86. Also I met our representative in Zambia, Mr Justin Gonakumoto who came all along from Zambia by bus. We discussed so many things with him concerning the work in Zambia. He told me that they are not safe if the church is not registered in Zambia. Also he told me that our Magazines are needed to be translated into Chichewa and Bemba languages so that the people can understand. This is also another problem in Malawi and Mozambique. They need the magazines to be translated in Chichewa so that all people can understand. I talked with both Mulozowa and Justine if they can do that work. They agree that they can do it perfectly. So Mulozowa want the current magazine so that he can start the translation. So please send it to Mulozowa. Since this work in these three countries is big and they are speaking the same language, I beg you pastor to assist so that they can print the magazines in Malawi. This will be safe and cheap. It will be so helpful to these countries.

## MEETING

After services I hold a meeting with all our hosts in Mozambique to discuss about the work in Mozambique. I wanted all of them to learn all the truths, I negotiated with Mulozowa that they with meet every month for three days to get teachings from our website and books because I took laptop to Mulozowa and they can use it. Next time when I will be going back I will carry laptop to Matiya and Justin. Another Pentecostal pastor came from northern part of Mozambique 300 miles away. He has been visiting our website frequently. So when he heard that I am in Mozambique, he came to meet me. we talked much and I told him that I will be back in Malawi in February or march And I will go to his place.

I have so many pictures for baptism and meeting. I will send them later and other in formations.

***– Evangelist Evans Ochieng***

As requested, the magazine was sent to Radson Mulozowa to get to of Zambia for translation. We have already produced a small amount of literature in Chichewa, but have never printed materials in Malawi before. Last February, I was able to personally meet Radson Mulozowa, Wedison Matiya, plus Hosea Baulen of Malawi. Currently, we are registered in Malawi and have been working on Mozambique registration

We had Justin Gonakumoto look into what we need to do to be 'legal' in Zambia (a country we still have not claimed to have congregations in, but may be able to do so some time this year). So after reviewing that, we sent some funds to work on registering the CCOG in Zambia. We also sent a small amount of funds for food for those in Malawi affected by the armyworms–and because of drought as well, we may to send more.

Furthermore, I told Evans Ochieng that we would support the printing of our magazine and other literature in Malawi (perhaps I should mention that Malawi is the second poorest nation on Earth according to a report that came out this month). Printing literature in Malawi should also help us better teach those in Mozambique and Zambia in accordance with Jesus' commission in Matthew 28:19-20.

***Here are two photographs that were sent:***



Malawi and Mozambique baptismal candidates



Mozambique children

***Below is a photograph of a congregation in Mozambique:***



# Kukwaniritsa Mateyu 24:14 ndi Mateyu 28:19-20



*Continuing* Church of God www.ccog.org
Daily *Bible News Prophecy* www.cogwriter.com

**CCOG.ASIA** Iyi ndi webusaitiyi yomwe ikuyang'ana ku Asia. Lili ndi zilembo mu Chimandarini cha China komanso zina mu Chingerezi, kuphatikizapo zinthu zina m'zinenero zina za ku Asia.
**CCOG.EU** Ili ndi webusaitiyi yomwe imalowera ku Ulaya. Lili ndi zipangizo m'zinenero zambiri za ku Ulaya.
**CCOG.IN** Ili ndi webusaitiyi yomwe ikukhudzidwa ndi ma Indian, ndipo ikuphatikiza zipangizo mu Chihindi.
**CCOG.NZ** Ili ndi webusaitiyi yomwe imalowera ku New Zealand.
**CCOGCanada.CA** Ili ndi webusaitiyi yomwe ikukhudzidwa ndi anthu a ku Canada.
**CDLIDD.ES** La Continuación de Iglesia de Dios. Ili ndi webusaiti yathu ya Chisipanishi ya Mpingo wopitiriza wa Mulungu.
**PNIND.PH** Patuloy na Iglesya ng Diyos. Iyi ndi webusaitiyi ya Philippines yomwe ili ndi zinthu zina mu Chingerezi ndi Tagalog.

---

YouTube

***BibleNewsProphecy channel***
*www.youtube.com/BibleNewsProphecy*

***ContinuingCOG channel***
*www.youtube.com/continuingcog*

***ContinuingCOG Africa channel***
*www.youtube.com/ccogafrica*

---

The *Continuing* Church of God CCOG imagwiritsanso ntchito makope osindikizidwa ndi apakompyuta, mabuku, ndi malembo a sabata kwa abale kuti azithandizira Mateyu 24:14 ndi Mateyu 28:19-20.